

WOPAMBANA MASTER CHING HAI

KIYI WA CHIDZIWITSO CHOPEZEKERATU
Kabukhu Kaulere

ZAMBUKUMU

WOPAMBANA MASTER CHING HAI	1
ZAMBUKUMU	2
MAU OYAMBIRIRA	4
MBIRI YA MASTER CHING HAI MWACHIDULE	7
ZINSINSI ZA DZIKO LIKUDZA	9
NTHAWI YAMAFUNSO CHIPHUNZITSO CHITATHA	22
MWAMBO:	30
NJIRA YA QUAN YIN	30
ZOYENERA KUTSATIRA ZISANU	31
UBWINO WODYA ZAKUDYA ZAMASAMBA	33
MASTER AYANKHA MAFUNSO	39
ZAMASAMBA	43
YANKHO LAVUTO LAKUSOWA KWA MADZI PADZIKO LONSE	43
UTHENGA WABWINO KWA ODYA MASAMBA	45
Puloteni yofunika yochokera ku masamba	45
ZOSINDIKIZA	53
Za pa Intaneti zokhudza Quan Yin	61
MUNGATIPEZE BWANJI	63

“Ine sindine wachiBuddha kapena wakatolika. Ine ndine wa chilungamo ndipo ndimalalika choonadi. Mukhoza kuchitcha chiBudha, Tao kapena china chirichose mungachitche ndimalandila zonse.

The Supreme Master Ching Hai

Tikapeza mtendere wamumtima ndi zonse. Kukhutitsidwa konse ndikukwaniritsidwa kwa zilakolako zadziko ndi zakumwamba zimachokera mu ufumu wa Mulungu-kuzindikira kwa mtima, chisangalalo ndi nzeru zosatha komanso mphamvu. Ngati sitipeza zimenezi, sitidzapeza kukhutitsidwa ngakhale tikhale ndi ndalama kapena udindo wina uliwonse.

The Supreme Master Ching Hai

Chiphunzitso chathu chimati chinalichose chimene tingachite “tichichite ndi mtima wathu wonse. Tikhale wokhululupirika ndinso tidzi lingalira tsiku lilonse. Mudzapeza nzeru zapadera, mtendere kuti mudzitumikire ndi dziko. Osaiwala kuti muli ndi ubwino mkati mwanu. Osaiwala kuti Mulungu amakhala mkati mwanu. Osaiwalanso kuti Mulungu amakhala mu mtima wanu.”

The Supreme Master Ching Hai

MAU OYAMBIRIRA

Kuyambira kalero, munthu pa dziko lapansi wakhala akuyenderedwa ndi anthu apadera kwambiri omwe cholinga chawo ndi kulimbikitsa uzimu pakati pa anthu. Yesu Khristu ndi mmodzi mwa alendowa. Monganso Shakyamuni, Buddha ndi ena mwa anthu amenewa. Atatu amenewa ndi amene ali otchuka koma alipo ena amene sitimawadziwa. Ena amaphunzitsa poyela koma ena samadziwika. Anthuwa amatchedwa maina osiyanasiyana kumalo osiyana ndi nthawi zosiyana. Akhala akutchedwa Master, Avata, Wosankhidwa, Mpulumutsi, Mesiya, Mai oyera, Mtumiki, Mtsogoleri, Woyera wamoyo ndi zina. Iwo anadza kudzatiuza za chipulumutso, kuzindikira, chidziwitso, kumasuka ndi kugalamuka. Mauwa akusiyana koma amatanthauza chinthu chimodzi.

Master Ching Hai ndi m'modzi mwa anthu amene amatengedwa kukhala senti wamoyo. Iye ndi mzimayi, ndipo maBuddha amakhulupilira kuti mzimayi sangakhale Buddha. Iye ndiwachimwenye koma anthu achiluya amayembekezera kuti mpulumutsi wao ali wachiluya. Koma ife ochokera kumaiko osiyanasiyana ndi zipembedzo zosiyana koma amene timamudziwa ndikutsata ziphunzitso zake, timadziwa chimene ali. Kuti mudziwe izi maganizo anu ayenera kukhala omasuka komaso olungama mumtima. Zikutengerani nthawi komaso chidwi.

Anthu amataya nthawi yao kupanga ndalama ndi kudzisamalira. Timagwila nchito kuti tifewetse moyo wathu ndi mabanja athu. Nthawi tikayipeza timakhala ndi chidwi ndi ndale, masewela, kanema kapena milandu. Kwa ife amene takhudzidwa ndi mphavu yachikondi chakudziwana ndi Woyerayo timadziwa kuti moyo sizokhazi. Timamva chisoni kuti uthenga wabwino siwofalikira. Yankho lamavuto athu liri mmitima mwathu, kutidikila. Timadziwa kuti kumwamba kuli pafupi. Tikhululukileni tikalankhula ndimphavu ndikunena zinthu zimene zikhoza kukukhumudwitsani. Ndi zovuta kuti tikhale chete kuona zimene zikuchitika ndikudziwa zimene timadziwa.

Ife amene timadzitenga ngati otsatila ake a Master Ching Hai komanso otsatila a njira ya Quin Yin tikukupatsani bukuli ndi chiyembekezo choti likubweretsani chikhutitso mwa Master wathu kapena wina.

Master Ching Hai amaphunzitsa za ubwino woganiza mwakuya ndi kudzisanthula mtima komanso pemphero. Iye

akufotokoza kuti tiyenera kuzindikila uzimu umene uli mkati mwathu ngati tili okondwa. Iye akuti chidziwitso sichosowa koma nchopezeka kwa iwo otuluka muzochitika za dziko. Ntchito yake ndikuutsa uzimu mwaife pamene tikhala moyo wabwino. Iye akuti zili ngati chonchi, timadziwa chilungamo koma tinaiwala. Ndithu nthawi zina munthu amayenera kutikumbutsa zacholinga cha moyo wathu ndikukhulupilila Mulungu kapena Buddha kapena amene timati ali ndi mphamvu mumlengalenga. Sakupempha kuti timutsatile, akungopeleka chitsanzo cha chidziwitso chake kuti ena akathe kumasulidwa.

Bukuli ndi chiyambi cha ziphunzitso za Master Ching Hai. Chonde dziwani kuti ziphunzitso, mau, miyambi yonenedwa ndi Master Ching Hai zomwe zalembedwa zinalankhulidwa ndi iye mwini koma zinamasulidwa muzilankhula zina nkukonzedwa kenako kusindikizidwa. Tikulimbikitsa kuti mumvere kapena kuonera matepi ake. Mudzapeza zambiri kusiyana ndibukuli. Komanso kuti mudziwe zambiri muyenera kumuona maso ndi maso.

Kwa ena Master Ching Hai ndi mai, kapena tate wao. Kwa ena ndi okonedwa. Iye ndibwenzi lapamtima limene mungapeze padziko. Anadza kudzatipatsa osati kudzatenga. Salandira malipilo ku ziphunzitso zake. Chinthu chimene angatenge kwa inu ndi mavuto, chisoni ndi kusweka mtima kwanu. Koma ngati inu mukufuna!

*****Uthenga Wochepa*****

Pokamba za Mulungu master akutilamula kuti tigwiritse mau opanda mwini, kuti tipewe mtsutso woti Mulungu ndi wammuna kapena wamkazi.

She + He = Hes (as in Bless)

Her + Him = Hirm (as in Firm)

Hers + His = Hiers (as in Dear)

Chitsanzo: Mulungu akamayankhula zomwe akufuna, Hes amapangitsa zinthu kuti zichitike monga mwa Hiers kuti zgwirizane ndi Hirmself.

Monga katswiri wa zolemba ndi zojambula komanso mphunzitsi wa zauzimu Master akutiphunzitsa za kukongola kwa mkati. Pachifukwa ichi iye amatchula dziko la Vietnam kuti "Au Lac" ndipo Taiwan kuti "Formosa". Au Lac ndi dzina la kale la Vietnam ndipo limatanthauza 'chimwemwe.

Ndinso Formosa limatanthauza 'wokongola' ndiposo limanenanso za kukongola kwa chilumbachi ndi anthu ake. Master amaona kuti kugwiritsa ntchito mainawa kumabweretsa kusunthika ndi mwai.

“Master ndi amene ali ndi upangili wokusandutsa master..... kukuthandiza kuzindikila kuti ndiwe master komaso kuti ndiwe mmodzi ndi Mulungu.Imeneyo ndiyo nchito ya master.”

The Supreme Master Ching Hai

“Njila yathuyi sichipembedzo.Ine sinditembenuza aliyese ku chiBuddha, chikatolika kapena zina. Ndimangopeleka njila yoti mudziwire komwe mukuchokera, nchtito yanu ,zisisi za chilengedwe, ndikumvetsetsa chifukwa chimene kuli chisoni chambili ndi zomwe zikudikila tikamwalila.

The Supreme Master Ching Hai

Talekana ndi Mulungu chifukwa chotanganidwa. Munthu akamatilankhula, lanya nkumalila, komaso mukuphika kapena kucheza ndi ena ndekuti palibe angalumikizane nanu. Ziliso chimodzimodzi ndi Mulungu Iye alikuitana tsiku ndi tsiku koma tilibe nthawi yomvetsera kwa Iye.

The Supreme Master Ching Hai

MBIRI YA MASTER CHING HAI MWACHIDULE

Master Ching Hai anabadwa mu banja lopeza bwino ku Au Lac. Iyeyu anali mwana wa mkulu wachipembedzo, anakula muchikatolika naphunzila za chiBuddha kuchokera kwa agogo ake. Monga mwana amaonetsa chidwi mu ziphunzitso zauzimu ndi umunthu komaso chidwi ndi chilengedwe. Ali ndi zaka khumi ndi zisanu ndi chitatu, iye anapita ku Mangalande kukachita maphunzilo kenako ku France komaso ku Jeremani kumene amagwira ntchito ku bungwe la Red Cross na kwatiwa ndi mwamuna wa konko amene amachita za kafukufuku wa sayansi.

Patapita zaka ziwiri ali mbanja komaso ndichilolezo cha mwamuna wake iye anasiya banja pofuna ‘chidziwitso’ kukwanilitsa nzeru imene amaifuna kuyambira ali mwana. Panthawi nkuti akuphunzila za njila ndi ziphunzitso za uzimu kwa aphunzitsi ndi master amene anali naye pafupi. Anazindikila kuperewera kwa nzeru za munthu komanso ntchito yokanika kuthandiza pawekha ndiye anafunitsitsa kuti apeza mpata wothandizila ena komanso kuyenera kudzidziwa wekha. Ichi chinakhala khumbo lake ndipo iye anayenda maiko osiyanasiyana kufuna “chidziwitso.”

Anadutsa mu zaka zamayetsero Master Ching Hai anapeza njira ya Quan Yin ndi ulendo wa uzimu ku Himalayas!. Patapita nthawi yachiyetselo ku aHaimalayasi iye analandila “chidziwitso.”

Papita zaka chilandilileni chidziwitso Master Ching Hai anakhala moyo wa chete wa mtumiki wachiBuddha. Ali wamanyazi, amasunga chiphunzitso mpaka pomwe amalankhula kwa anthu omwe amafuna malangizo ndi mwambo. Chifukwa cha pempho lochokera kwa omutsatira ku Formosa ndi ku Amerika Master Ching Hai waphunzitsa mmalo osiyanasiyana, nupatsa mwambo kwa anthu zikwizikwi. Lelolino anthu ambili ofuna choonadi amapita kwa iye kukafuna nzeru zake . Kwa iwo ofuna ofuna kuphunzira njila ya”chidziwitso” imenne li mwambo wa Quin yin iye ali wolola kupeleka mwambo ndi nzeru zauzimu.

*Dziko ladzadza ndi mavuto
 Koma ine ndadzadzidwa ndi Inu
 Mukanakhala mkati mwa dziko
 Mavuto onse akanatha
 Koma dziko ladzadza ndi mavuto,
 Ndipo ndilibe nthawi nanu*

*Ndikanagulitsa dzuwa , mwezi ndi nyenyezi
 Mumlengalenga
 Kuti ndigule limodzi maonedwe anu
 O Master wa kukongola kozwizwitsa
 Khalani ndichisomo nundi patsa chimwemwe chamumtima
 wanga wosweka*

*Anthu adziko amaimba nuvina usiku
 Mukuwala kwa dziko ndi nyimbo zadziko
 Ine ndekha ndikhala odala
 Kuvina ndi chimwemwe chamumtima*

*Nditangodziwa ulemelelo wanu Mbuye
 Sindingakonde zadzikoli
 Ndikumbatileni mchikondi cha chisomo chanu
 Kwamuyaya!
 Amen*

*Kuchokera 'misozi yamumtima'
 ndakatulo yolembedwa ndi Master Ching Hai*

ZINSINSI ZA DZIKO LIKUDZA

Chiphunzitso cha Master Ching Hai pa

June 26, 1992, ku United Nations mu mzinda wa New York

June 26, 1992 (DVD#260)

United Nations, New York

(Originally in English)

Mwalandiridwa kuno ku United Nations chonde pempherani limodzi kwa mphindi zochepa muchipembedzo chanu kuti tathokoza pazomwe tilinazo, tapatsidwa nufuna kuti iwo amene alibe akapatsidwa ngati ife kwa othawa nkondo, okhudzidwa ndi nkondo, asilikali, atsogoleli a boma ndi atsogoleli a United Nations kuti akakwaniritse zofuna zao ndikukhala mu mtendere.

Timakhulupilila kuti tikapempha tidzapatsidwa tidzalandila chifukwa Baibulo limatero. Zikomo!

Monga mukudziwira mutu wathu lero ndi “dziko lilinkukudza” chifukwa sindingafune kunena za dziko lino zomwe inu nonse mukudziwa. Koma mdziko limene likudza muli zinthu zina. Ndikudziwa kuti nonse mwabwera kuno mukhoza kufuna kudziwa. Sichinthu ngati ananena mzathu za zozwizwitsa kapena zinsinsi zimene simungakhulupilile. Ndi chinthu chofunika, cholondola ndi choona.

Tamva kuti mabuku achipembedzo munenedwa kuti kuli kumwamba asanu ndi awili, kulinso kaganizidwe kaumunthu kosiyana. Kuli ufumu wa Mulungu mmene muli Buddha ndi ena. Izi ndi zina zolonjezedwa mu dziko likudza. Koma ambili sapeza mpata wodziwa zolembedwa mmawu opatulika. Kutengera chiwerengero cha dziko anthu odziwa izi ndi ochepa.

Ngati muli ku America muli ndi mwai wowerenga mabuku ambiri okamamba zadziko limene likudza. Mafilimu ena amene anthu aku Amerika amapanga siabodza ayi enanso anapangidwa ndi anthu aku Japan. Chifukwa anthuwa anawerenga mabuku olembedwa ndi anthu amene anapita ku dziko limene likudza kapena iwo eni anaonako ufumu wa Mulungu.

Kodi muufumu wa Mulungu mulinji? Kodi tivutikilani ndi ufumu wa Mulungu ngati tili ndi nchito yoti tigwile padziko, tili ndi nyumba zotetezeka, maubale olimba ndi zina? Chifukwa tili ndi zonsezi tiyenera kukhudzidwa ndi ufumu wa Mulungu.

Zimamveka zokokomeza tikati ufumu wa Mulungu. Koma ndi njila yoganizila ya pamwamba. Anthu akale amati kumwamba koma tikhoza kunena kuti kaganizidwe, nzeru zapamwamba. Ndipo tikhoza kufikako ngati tidziwa kafikidwe kake

Posachedwapa tinamva kuti ku Amerika anapanga makina amene akhoza kukuikani mu samadhi. Kodi izi zinayamba zakuchitikilani? Chiliko ku Amerika pamalonda. Kaya mufuna zala mazana asanu kapena zisanu ndi ziwiri. Akutcha ichi njila yoti anthu aulesi ndi mmbindikilo akhale mu samadhi. Ngati simudzira ndifotokozapo pazimenezi.

Akuti makinawa akhoza kukuikani munjira yopumulila ndikukuonjezerani zeru. Zikuyenera kukupatsani nzeru, umunthu ndikumvetsa bwino. Makinawa magwilitsa nchito nyimbo, nde mumafunika maiyefoni kenako mulumikiza kumagetsi kenako mumaona ziwaliwali. Mumafunikaso chophibila mmaso. Zimenezi nzimene mumafunika mu samadhi. Makinawa ndiabwino komaso ali pamtengo wa mazana anayi okha basi. Koma njila yathu ndiyo yotchipa simufunika ndalama komaso ndiyamuyaya. Simuyenera kutchaja mabatile kapena magetsi, kapena kukonzetsa ikaonongeka.

Tsono ngati nyimbo ndi kuwala zimapatsa munthu nzeru zikuyenera kuwapatsa, sindinayesereko koma ndinawerenga mu nyuzi. Nchifukwa makinawa akuyenda malonda. Ngati zinthu zopangidwa ndi munthu zimaonjezera nzeru nanga bwanji chenichenicho? Chenichenicho chili mudziko limene likudza koma nchopezeka kwa aliyese ngati tichifuna. Izitu ndi nyimbo zakumwamba ndi mvekero wamumtima. Kutengera ndi kafulumilidwe ka nyimbo tikhoza kudzitengera kumalingalilo akuya akaganizidwe.

Ndiyesa zimangokhala ngati lamulo lazinthu za phunzilo la fizikisi (sayansi). Kuti ngati mufuna kutumiza ndege mumlengalenga

pakuyenera kukhala mphamvu zambili ndiposo ikauluka imatulutsa kuwala. Ndikhulupilila kuti tikalowa mudziko limene likudza tikhoza kuonetsa kuwala komaso tikhoza kumva.

Kamvekedwe kameneka ndikamene kamati sunthila ife kumalo okwera koma izi zimachitika popanda phokoso, zovuta zilizonse, mtengo, komaso kumangika kwa ochitikidwa. Imeneyi nde njira yopitila muzakudza. Kodi mulinji chimene chili choposa cha dziko lino? Zonse zimene tikhoza kuganiza ndi zimene sitingathe. Zikatichitikila ndipamene timadziwa. Palibe amene angatiuze. Koma tiyenera kukhala olimbika chifukwa palibe wina angatichitile.

Chimodzimodzi ndi munthu wina kutenga malo anu antchito nkulipidwa. Monganso munthu wina kudya ife nkukhuta. Chonchoso njilayi iyenera kutsatidwa. Tikhoza kumvera kwa amene zinawachitikila, koma sitingadziwe zambili kudzera mmenemo. Tikhoza kudziwa kamodzi kapena kangapo kutengera mphamvu yamunthu amene wakumana ndi Mulungu kenako timaona kuwala kapena timamva mau popanda khama lathu koma sakhalitsa ndiye tiyenera kuyesa patokha.

Mudziko likudza muli maiko osiyanasiyana. Mwachitsanzo monga iye ali wopambana kuposa ife. Chimene timatcha kuti dziko la Astra. Mudziko la Astra muli milingo yoposera makumi khumi. Ndipo mulingo uliwose ndi dziko palokha. Ndipo limaimila mlingo wa kaganizidwe kathu. Monga tikapita kusukulu yaukanjede, timakwera zaka zikamapita, zimaimila kaganizidwe kathu, komaso zophunzila zimachulukuka kenako timamaliza ndikupanga galajuweti..

Mudziko la Astra timaona zozwizwitsa ndipo timayesedwa ndizozwizwitsazi ndipo ifenso tikhoza kukhala nazo. Tikhoza kuchiza munthu, nthawi zina kuona zinthu zimene ena sangaone. Tili ndi mitundu isanu ndi imodzi ya mphamvu yochitila zozwizwitsa. Tikhoza kuona kuposera zomwe maso angathe kapena kumva zimene zili mumlengalenga. Utali umene ulipo siutanthauza chilichose kwa ife. Zimenezo ndizimene timazitcha maso ndi makutu zakumwamba. Penanso timatha kuona zomwe zili mmaganizo a ena. Zimenezi ndi mphamvu zimene timapeza tikafika mumlingo woyamba waufumu waMulungu.

Mkati mwamlingo woyambawu, ndanena kale kuti tili ndi milingo yambili imene mau sangathe kufotokoza. Mwa chitsanzo ukatha mwambo kenako nkubindikila komaso ngati tili mumlingo woyambilira ndekuti timakhala ndi mpata wochita zinthu zambiri. Timathaso kukonza kalankhulidwe kamene tinalibe. Komaso timadziwa zinthu zimene anthu samadziwa pena kulandira mphatso zochokera kumwamba ku mbali yazachuma, ntchito ndi zina zambiri. Kenako timayamba kulemba ndakatulo ndikujambula zithunzi ndikumapanga zinthu zimene sitinapangapo kapena kuganizirapo. Umenewo nde mlingo woyamba. Ndipo tikhoza kulemba ndakatulo ndi mabuku mwaluso. Tikhoza osakhala mlembi koma nkulemba mwa ukatswiri. Zimenezi ndi zina mwa zinthu zimene tingapeze tikakhala mumlingo woyambilira.

Zimenezi simphatso za Mulungu. Zinthuzi zili kumwamba mkati mwathu koma chifukwa tazitsitsimutsa izo zakhala zamoyo. Kenako tikhoza kuzigwilitsa ntchito. Zimenezi nde zina za mlingo woyambilira.

Kenako timapita ku mlingo wokwera, timaona zinthu zambiri ndi kukwaniritsa zina. Malinga ndi nthawi sindikwanitsa kukuuzani zonse. Sibwinoso kumva zakakomedwe ka mkate koma osaudya. Ndendimango utsa mudyo ngati mufuna kudya imeneyo ndi nkhani ina. Tikhoza kupeleka chakudya chenicheni patsogolo. Inde mwina mufuna kudya zinthuzi.

Tsono ngati tipita kumlingo wachiwiri tayenera kukhala ndi upangili woposera woyamba monga zozwizwitsa. Koma chosililika chimene tingapeze mumlingowu ndikuthekera kwa mtsutso. Palibe munthu amene angagonjetse iye amene ali mumlingo wachiwili chifukwa iye ali kafotokozedwe kopambana akakhala pachimake cha mphamvu.

Anthu ambiri amene ali ndimaganizidwe ochepa sangafane ndi munthu wotele chifukwa nzeru zake zimakhala zitamasuka kufika poonjezekera. Siubongo wokha umene umakhala utamasuka, imakhala mphamvu yakumwamba ndi nzeru zomwe zimakhala mwa ife. Tsopano zimayamba kumasuka. Ku India anthu amatcha mlingowu "Buddhi" kutanthauza mlingo womasuka. Ukafika pa "Buddhi" umasanduka "Buddha", pamene ndi pamene mau oti Buddha

anachokera kumau oti buddhi. Ine ndikudziwitsani za Buddha yekha basi koma kuli zina zoposera apo.

Anthu amatcha munthu wachidziwitso kuti Buddha. Ngati sadziwa zoposera pamlingo wachiwiri ndiye akhoza kunyadila, nkuganiza kuti iye ndi Buddha wamoyo ndipo omutsatila ake akumamutcha Buddha. Koma ngati akwaniliritsa mlingo wachiwiri iye akhoza kuona kale tsogolo komanso zatsopano za amene iye afuna komanso kamasukidwe kalankhulidwe ndesimathero a ufumu wa Mulungu.

Munthu aliyese asanyadire mphatso yake yowerenga mbili zakale, zamtsogolo komanso zapompano zimenezi nde mbiri za “Akashic” monga mmene amtchulira kumaiko akummwera. Nonse amene mumatsata m'bindikiro kapena yoga mukhoza kumvetsetsa mbiri ya akashic, imene ili ngati nyumba yosungira mabuku monga imene yagundizana ndi UN imene ili ndizilankhulo zosiyanasiyana. Mumapezamo chiArabia, chiRasha, chiChaina, Chingerezi, Chifuransa, Chijeremane zonse monga munyumba tagundizana nayo. Ngati mukhoza kuwerenga zilankhulo zonsezi nde mukudziwa zimene zikuchitika mmaiko ake. Chimodzimodzi iye amene angafike pamlingo wachiwiri amamvatsetsa ndi kumasulira njira zamunthu monga mmene timaonera mbiri yathu yomwe.

Pali zambiri zomwe tingapeze pamlingo wachiwiri. Koma munthu akafika mlingo wachiwiri amakhala ali Buddha chifukwa umakhala utatsegula buddhi. Ndipo timadziwa zinthu zambiri zimene sitingathe kuzitchula. Ndipo zozwizwitsa zikhoza kutichikira kaya tifuna kapena ayi chifukwa kamasukidwe kathu katseguka ndipo kadziwa kalumikizandwe ndi mphamvu yamachiritso yakakonzedwe kuti moyo wathu ukhale wabwino ndi wokoma. Ndipo buddhi yathu imakhala itatseguka ndipo ikhoza kufufuza ndikulongedza zonse zoipa zimene tinapanga mmbuyo. Kuti tikonze zolakwikazo nkukonza moyo wathu kuti ukhale bwino.

Mwachitsanzo ngati sitinadziwe kuti takhumudwitsa anzathu osati mwadala nde pano tadziwa. Zophweka, ngati sitikudziwa ndipo nzathu akusinkha kuchita chinachake chotibwezera koma pano tikudziwa chifukwa chomwe chinachitikira. Nde ndi zosavuta tikhoza kupita, kutchaya thenifolo kapena kumuitanitsa mzathuyo nkukambirana kuti

tithetse mkangano.

Molingana ndi mmene timachitila tikafika pamlingo womasuka mwachifatse timatha kumvetsa ndikuzilinganiza kapena kulumikizana ndi mphamvu imene ikhoza kutithandiza kuti moyo wathu usinthe nde timachepetsa ngozi, ndi zosalakika zina zamumoyo wathu. Tsono tikafika mlingo wachiwiri zimakhala kale zinthu zosangalatsa.

Zimene ndafotokozazi ndizochitika komaso zoon. Palibe chifukwa choganizira kuti munthu wochita mmbindikiro ndi yoga ndimunthu wamphamvu zapadera. Ali apadera monga ena mwa ife amene tatukuka chifukwa tikudziwa.

Ku Amerika timanena kuti chilichonse chimatengera ndi zimene timadziwa nde tikhoza kuphunzira chirichonse. Tsono zimenezi zili ngati sayansi ya dziko limene likudza mmene tikhozanso kuphunzira. Zimaoneka zodabwitsa koma, ngati zinthu zinka nukwerera ndekuti zinkaso zikuphweka. Ndizophweka kusiyana ndikupita kusukulu za ukachenjede ndi zasekondale ndi masamu osokonekera.

Mkati mwa mlingo wachiwiri muli magawo osiyanasiyana. Koma ndizichepetsa chifukwa sindingathe kudziwa zinsinsi zonse zakumwamba. Mukhoza zinthuzi mutayenda ndi Masta amene anayendapo kale njilayi. Nde palibe chinsinsi koma ndiyayitali zedi ngati tidutsa mlingo uliwonse umene ulinso ndi magawo angapo ndetiyangana chirichose zimatenga nthawi. Nde nthawi zina master amangokutengera kumilingo yosiyanasiyana mwachindunji mwamsanga. Ngati ulibe chidwi ndizauMasta nde palibe chifukwa chophunzilira zonsezi. Nde amangodutsitsa ndi kukubweretsanso chifukwabe zimatenga nthawi. Nthawi zina zikhoza kutenga moyo wathu wonse. Koma chidziwitso timachipeza pompo.

Koma chimenechi ndichiyambi chabe monga kulembetsa. Tsiku loyamba kusukulu timalembetsa tikatero timakhala wophunzira wapasukuluyo. Koma zikusiyana ndi Ph.D. pakapita zaka zisanu ndi chimodzi, zinayi kapena khumi ndi ziwiri kenako timapanga galajuweti. Koma ngati ukhala wophunzira pasukulu, ngati ili sukulu yamphamvu ukangolembetsa ndekuti wafunitsitsa kukhala wophunzira. Nde mbali zonse ziwiri ziyenera kugwirizana.

Mongaso ngati tifuna kupita koposa dziko lino mwachitsanzo mwina kokasangalala chifukwa tilibe kopita kuno ku New York tadziwa zonse zaku Manhatani. Nde tingo ganiza kuti tifuna kupita kumalo opuma kuti tikaone zimene zikuchitika. Poti timalipila ndalama zambiri popita ku Miami kuti tikasambire nde bwanji nthawi zina sitingangopita mmaiko ena oposela dziko lino kutitikaone mmene zolengedwa zina zimaonekera ndikukhalira. Sindikuona chachilendo ndizimenezi. Ayi? Ndi ulendo wakaganizidwe, uzimu mmalo mwa thupi. Pali mitundu iwiri ya ulendo. Nde ndizophweka kuzimvetsetsa.

Tsopano, tili pa mlingo wachiwiri, ndinene chiyani? Ndimmene timapitilizila pa dziko pano, koma tili ndi mbiri yamaiko ena nthawi imodzi. Chifukwa timayenda.

Monga ukakhala mzika ya ku Amerika kapena dziko linalililonse nde umayenda kupita kumaiko ena kuti ukaone mmene maikowo amaonekera. Komaso ndikhoza kuona kuti ambiri mwa inu muli muno simbadwa zakuno ku Amerika. Ayi kapena Eya. Tsopano nonse mwadziwa chinthu chimodzi. Tikhoza kupita kudziko lina kapena mlingo wina wamoyo kuti timvetsetse chifukwa chakutalika sitingathe kuyenda kapena kukwera roketi.

Maiko ena alipatali zedi moto olo UFO siingafike. UFO chinthu chosadziwika, chouluka. Tsono tilinawo upangili mkati mwathu umene uli wachangu kuposera UFO. Umene uli mzimu wathu. Ndipo tikhoza kuuluka popanda mafuta, polisi, kapena chilichose chotipinga. Sitingadandaule kuti aluya asiya kuti gulitsa mafuta. Chifukwa ndiopezekeratu. Samatha pokhapokha ngati tifuna kuononga pochita zosiyana ndi chigwirizano cha kumwamba ndi dziko lapansi zimene zisali zovuta kupewa. Tikuwuzani zambiri ngati mufuna.

Mwachitsanzo, ndichita chindunji sindine mlaliki. Osadandaula sindikupititsani kutchalitchi mwachitsanzo.

Pali malamulo ena a chilengedwe amene tiyenera kudziwa monga tikamayendetsa galimoto tiyenera kudziwa malamulo apa mseu. Getsi lofiila limati uyime, lobiliwira nyamuka. Nde kulinsu malamulo

achilengedwe aku thupi. Kupyolera dziko lino kulibe malamulo. Tili afulu ndi omasuka koma tiyenera kudutsa dziko lino kuti tikhale afulu. Koma ngati tili mudziko lino muthupi lino tiyenera kuyesetsa kusunga malamulo kuti tisagwe mmavuto. Kuti magalimoto athu asanonongeke kutiso tiuluke mothamanga opanda mavuto.

Tsono malamulowa analembedwa mu Baibulo la Chikhristu, chiBuddha ndi chiHindu. Zosavuta ngati osafunira nzako zoipa, osapha, osaba ,osapanga chigololo komanso osamwa zoledzeletsa. Buddha ayenera kuti anadziwa kuti muzaka zama 2000 anthu tipanga kokeni. Ndiye iye analetsa zozunguza bongo. Zozunguza bongo zikuphatikizaso njuga ndi chilichonse chimene chikhoza kutipanga kuti tizikonda zosangalatsa thupi nku iwala ulendo wauzimu.

Palinso malamulo ngati mufuna kuuluka mwaliwiro opanda zovuta komanso ngozi. Roketi ikafuna kuuluka woipanga amayenera kutsata malamulo ena. Nde tiyenera kusamalitsitsa chifukwa tikufuna kudutsa pamenepo.Tikufuna kudutsa maroketi ndi ma UFO. Koma pali zina zofunika kuzifotokoza ngati mungasangalitsidwe imeneyo idzakhala nthawi ya mwambo. Sitikufuna kukutopetsani ndizofunika kutsata zonsezi zimene mukhoza kunena kuti mukuzidziwa kale ndinaziwerenga mu Baibulo pa malamulo khumi.

Ambiri mwa ife tinawawerenga koma sitiwamvetse. Kapena timafuna kuwamvera mmene tifunira osati zimene atanthauza. Nde sizolakwika kutikumbutsa kapena kumvera kumvera tanthauzo lakuya lina. Mwachitsanzo mu Baibulo chipangano chakale tsamba loyamba Mulungu akuti analenga nyama kuti zikhale bwenzi lathu ndi mthandizi kuti muzilamulire. Nde akuti anapanga chakudya cha nyama zosiyanasiyana . Koma sanatiuze kuti tizidy. Akupitiliza kunena kuti anapanga zomera, zipatso zakudya zamNthaka zimene zili zokoma mmaso. Zimenezi zidzakhala chakudya chanu koma anthu ambiri samalingalira zimenezi choncho ambiri otsata Baibulo amadya nyama osamvesetsa chimene Mulungu amatanthauza.

Kafukufuku wa sayansi amatitsimikizira kuti sitiyenera kudya nyama. Thupi lathu, matumbo, mano, mamba zathu zinapangidwa kuti tizidya zamasamba zokha. Chifukwa chake anthu ambiri amadwala, kalamba,

kutopa, ngakhale anabadwa amphamvu ndi nzeru. Nde amanka nzeru zikuhepera nchifukwa munthu akamakalamba amamva kuipa za iye mwini. Nchifukwa choti timaononga zoyendera zathu nde ngati tifuna kuzigwiritsa ntchito kwa nthawi yaitali tiyenera kuzisamala.

Mwachitsanzo tili ndi galimoto. Nonse mumayendetsa magalimoto. Ndengati muika mafuta olakwika chinga chitike nchiyani? Ikhoza kuyenda mtunda waufupi kenako nkuima. Nde sumanena galimoto koma mafuta olakwika amene waikamo. Kapena ngati mafuta athu ali ndi madzi ikhoza kuyenda kenako nkuima. Kapena mafuta athu ali ndi dothi nde sitinawakonze ikhoza kuyenda koma iyima. Nthawi zina ikhoza kuyaka moto chifukwa sitinayisamale mokwanira.

Chimodzimodzi thupi lathu liri ngati galimoto imene tikhoza kugwiritsa ntchito ulendo wa kumwamba. Koma nthawi zina timaliwononga ndi kuigwiritsa ntchito pazinthu zolakwika. Mwachitsanzo galimoto yathu layenera kuyenda mitunda itali itali kuti pititsa kuntchito, kwa anzathu ndikumalo ambiri. Koma sitisamala timaikamo mafuta olakwika, sitionanso mosungila madzi ndi zambiri. Nde imasiya kuthamanga kwa mitunda italiitali. Ndetimango zungulira mmakomo mwathu. Ndizabwino koma kutaya cholinga chimene tinagulira galimoto, ndalama komaso nthawi ndi mphamvu zathu. Palibenso mlandu kwa apolisi, sangakulipilitsani chifukwa chazimenezo. Timangotaya ndalama zathu tikapita kutali nkukaona zinthu zambiri nkukasangalala.

Monganso matupi athu. Tikhoza kukhala dziko lino nkumadzisamala zonse zamkati mwathu chifukwa tili ndi zida zimene tikhoza kuyendetsa kupatula apo. Monga woyendetsa roketi amakhala mkati mwa roketiyo imene ili chida chake. Ayenera kusamala kuti asaswe malamulo a sayansi kuti ayende bwino ndi liwiro. Koma woyendetsayo ndi wofunika chifukwa roketi ikangomufikitsa kumene iye akupita. Chifukwa roketi siyofunikira koma woyendetsa ndikumene akupita. Koma ngati agwiritsa ntchito kuti angozungulila ku chilumba cha Long ndekuti wataya nthawi komaso ndalama za dziko.

Tsono matupi athu ndi amtengo wapatali chifukwa mwa ife ndimmene master amakhala. Nchifukwa chake Baibulo limanena kuti simudziwa kodi kuti ndinu kachisi wa Mulungu? Kutiso Mulungu amakhala mwainu chimodzimodzi Mzimu Woyera. Ngati Mzimu Woyera akhala mkati

mwathu talingalirani mmene izi zilili zovuta. Koma anthu ambiri amangowerenga osamvetsetsa zimene zikutanthauza. Nchifukwa chake onditsatira amakonda ziphunzitso zanga chifukwa akhoza kufufuza amene amakhala mkati mwathu ndizimene zili mudziko lija kupatula mavuto athu atsiku ndi tsiku.

Tili ndi kukongola, ufulu, nzeru zochuluka mkati mwathu. Ndiye tiyenera kudziwa njira yoyenera yofikira kuzimenezi. Zonsezi ndi zathu chifukwa zili mkati mwathu. Nchifukwa choti sitidziwa kumene makiyi ali nde takhoma nyumbayi kwa nthawi yayitali nde taiwala kuti tili ndi chinthu cha mtengo wapatalichi.

Nde iwo wotchedwa Master ndiamene akhoza kutithandiza kutsegula khomo ndikutionetsa zimene zili zathu. Koma tiyenera kukhala ndi nthawi yoti tilowemo ndi kuona ngati zonse zili momwemo .

Tsono tinali mudziko lachiwiri. Kodi ndinu osangalatsidwa kuti tinke patsogolo? (Inde! Inde!) Mukufuna kudziwa zonse osagwilira ntchito? Chabwino. Komabe munthu akhoza kukuuzani zakaonekedwe ka dziko lina ngati anapitako. Mwina mukhoza kukhala osangalatsidwa ngati mungafune kupitako. Chabwino tikachoka kudziko lachiwiri sindinamalize koma mukudziwa kuti sitingakhale muno kwa tsiku lonse. Tikachoka lachiwiri umakhala ndi mphamvu zochuluka. Ngati watsimikizika nulimbikira umapita kulachitatu. Dziko lachitatuli ndi mlingo wapamwamba.

Amene apita kudziko lachitatu ayenera kukhala wopanda ngongole ina iliyonse ya dziko lino. Ngati tili ndi ngongole ndi fumu ya dziko lino nde sitingathe kupita mwamba. Ngati ukakhala mkaidi wadziko lina ulibe chilolezo cholowa dziko lina. Nde ngongole ya dziko lina ili monga zinthu zimene unapanga mbuyo ndi pano mwinaso mtsogolo la moyo wathu. Zonsezi zikuyenera kubwezedwa monga timalipilira msonkho tisanalowe mdziko lina. Koma ngati tili mudziko lachiwiri timayamba kugwiritsa ntchito Karma yotsalira ya moyo wathu wakale ndi watsopano chifukwa popanda Karma yakale sitingakhale mmoyo uno.

MaMasta ali mmagulu awiri. Mmodzi wopanda Karma koma ambwereka Karma kuti itsike, winayo ali ngati ife anthu chabe koma a Karma yoyeletsedwa. Nde aliyense akhoza kukhala Masta. Nthawi

zina Masta amatsika kuchokera kudziko lapamwamba ndi Karma jobwereka. Inu mwazimva bwanji kubwereka Karma? Ndizotheka.

Mwachitsanzo, musanabwere pasi pano munali mutabwerapo kale. Komaso mwapereka ndikutenga ndi anthu osiyanasiyana kwa zaka zikwizikwi. Ndeno munapita kumwamba kapena kumpumulo kumene kuli kutali, milingiyo yosiyana ngati mlingo wachisanu. Imeneyo nde nyumba yaMasta mlingo wachisanu. Koma kupyola pamenepe pali milingo ina.

Tsopano, tikafuna kubwerera chifukwa cha chikondi cha Mulungu mwachitsanzo. Nde timabwera pansu. Koma chifukwa chakuchuluka kwa anthu ambuyo tikhoza kubwereka Karma . Ngongole yokha basi palibe chabwino cha anthu ake. Tikhoza kutenga ngongole ndikuibweza ndi mphamvu tuzimu pang'onopang'ono mpaka titamaliza ntchito yathu padziko lino.Tsono uwu ndi mtundu wina wa Masta.Komaso pali ena amena ali adziko lino akangoyesera nthawi yomweyo amakhala Masta. Monga kusukulu kumakhala aphunzitsi ndi ophunzira, amene akamaliza maphunziro awo akhoza kukhala aphunzitsi. Pali aphunzitsi akalekale komaso atsopano. Chimodzimodzi pali mitundu imeneyi ya maMasta.

Ngati tifuna kupita kudziko lachitatu tiyenera tikhale opanda Karma ili yonse. Karma ndi lamulo loti umakolola zomwe umadzala. Ngati timadzala malalanje timathyolaso malalanje, maapozi timapezaso maapozi. Ichi ndi chilankhulo cha chi Sanskrit cha cholinga. Baibulo sikamba za Karma koma limati udzakolola zomwe udzala zimene zili chimodzimodzi.

Baibulo lili ndi ziphunzitso zofupikitsidwa za Masta amenenso moyo wake unali wofupikitsidwa. Chonchonso Baibulo lilibe zofotokoza zambiri. Mafotokozedwe a Baibulo asinthidwa kuti agwirizane ndi atsogoleri a magulu amenewa, amene si anthu azauzimu nthawi zonse. Mukudziwa kuti muchinthu chilichonse anthu amagulitsa ndikugula. Koma Baibulo lenileni ndilosiyana pang'ono, lalitalipo, ndi losavuta kumvetsa. Nde poti tilibe umboni wake weniweni sitimalikamba pooa kuti anthu angati tikuwanamiza. Kuti tikambe zokhazo zimene tikhoza kupereka umboni.

Nde mukanandi funsa kuti "mumakamba za dziko lachiwiri, lachinayi komaso lachitatu umboni wake ndiwotani?" Ndikhoza kupereka umboni. Ngati muyenda limodzi nane mnjira imodzi tidzaona zinthu zimodzi. Koma ngati simungayende nde sindingapereke umboni. Nchifukwa ndimakamba zazinthuzi chifukwa zili ndi umboni. Pamodzi otsatila mazana mazana tili ndi umboni. Nde tikhoza kukamba zinthu zimene tikuzidziwa. Koma izi muyenera kuyenda nane chifukwa simungati ndikuyendereni nkukufotokozerani zonse chifukwa sindichite.

Mwachitsanzo ngati sindiri ku United Nations mchipinda chino palibe chaphindu ndi maonekedwe achipindachi. Izi sizinandichitikirepo. Ndetiyenera kuyenda ndi mtsogoleri wodziwa. Ndilinso ndi otsatira ochokera mmiko osiyanasiyana mchipinda chino akhudzidwa ndi zina zimene ndafotokozazi.

Dziko lachitatu likatha palibe chilichonse. Zimene ndakuuzani ndi gawo lazonse. Ngati nkhani yolumikizitsa zinthu koma osafotokoza zonse. Tikawerenga buku lokhudza dziko lina silimakhala dzikolo. Tawerenga mabuku ambiri akayendedwe ndi maiko koma timakonda kupita kumaloko tokha. Timadziwa za Spain, Tenerife, Greece koma zimenezi ndizammabuku basi. Tiyenera kupitako tokha nkukadzionera zakudya, anthu, nyengo ndi madzi anyanja zakumeneko.

Nde nanga ukafika dziko lachitatu chimachitika nchiyani? Umapita mmwamba nkupita kudziko lachinayi limene lili lodabwitsa. Sitingathe kugwiritsa ntchito mau chabe pofotokoza poopa kulakwira mbuye wadzikoli. Chifukwa dzikoli ndi lokongola kwambiri ngakhale liri ndi malo ena amdima. Koma tisanafike nkuwala mdima ndi wowirira zedi uli ngati mzinda woletsedwa. Tisanafike kunzeru za Mulungu timaimitsidwa kumeneko. Koma ndi Masta wozolowera mukhoza kudutsa koma nokha simungapeze njira mumdima wotere.

Tikafika pamalo osiyana timaona kusunthika kwa uzimu, kuthupi ndi chinachilichonse mmoyo wathu. Timaona moyo njira yosiyana, komaso timasintha kayendedwe ndi kagwiridwe kathu ka ntchito. Ingakhale ntchito yathu imasintha tanthauzo yake kwa ife, nde timamvetsa chifukwa chimene timagwirira ntchito.

Timamvetsetsa cholinga cha moyo wathu nde timalaka kulema ndi kuthodwa. Komaso timayembekeza mosawilingula nthawi imene ntchito yathu padziko lino idzathe chifukwa tikudziwa kumene tidzapite. Timadziwa izi chufukwa tikadali ndi moyo. Nzimene zimatanthauzidwa tikamati kufa uli ndi moyo. Ndikhulupilira ena mwa inu munamvapo zaizi koma sindikudziwa Masta amene angalankhule mosiyana kupatula kuti tiyenera kumva chimwemwe cha masophenya.

Munthu wina agafotokoze zaa benzi mosiyana? Zikuyenera kukhala chinthu chimodzi. Nde anthu amene ali ndi benzi ndikuidziwa akhoza kufotokoza zimodzi koma zimenezi si benzi. Nde ngakhale ndikukulankhulani mophweka koma zimenezi sizapafupi tikuyenera kuzichita tokha, ndi ntchito komaso ndi mtsogozzi. Ngakhale tikhoza kudzazichita tokha koma ndi kusamala chifukwa tikhoza kupeza zotsatira zosalakika.

Anthu ena akale Swedenvorg anadzipanga okha. Kapena Gurdjieff amene akanazipanga anapita yekha. Koma ndikawerenga mabuku palibe mwaiwo amene akhala opanda zozunza ndi zovuta. Sizofunikira kuti afike mlingo wokweretsa.

Ukachoka umapita pa mlingo wokwererapo. Ukachoka pamlingo wachinayi umapita mnyumba ya Masta imene ili mlingo wachisanu. Mamsta onse amachokera kumeneko. Ngakhale milingo yawo ili yokwererapo amakhala pompo. Nkumalo kokhala maMasta. Kupyolera pamenepo pali nthambi zambari zaMulungu amene ali ovuta kuwamvetsetsa. Sindikufuna kukusokonezani nde ndidzafotokoza nthawi ina mwina mwambo utatha chifukwa mudzakhala mutakonzeka ndipo ndidzakuuzani za maganizidwe anu mmene nthawi zina amaganiza molakwika za Mulungu.

NTHAWI YAMAFUNSO CHIPHUNZITSO CHITATHA

Q: Munanena kuti master akhoza kubwereka Karma ya anthu. Nanga ngati Karma yafufutika chimawachitikila anthu nchiyani?

M: Master akhoza kufufuta Karma yaaliyense. Ngati zimenezo zili zimene afuna kuchita. Otsatira onse panthawi ya mwambo Karma ya kale imafufutika. Ndimangokusiyirani Karma yapanoyi. Kuti tipitilire ndi moyo. Palibe Karma ingakhale pano. Nde Masta akuyenera kufufuta Karma yosungidwa iliyonse kuti munthuyo ayeretsedwe nkumusiyira Karma pang'ono kuti apitilire ndi moyo ndikugwira ntchito yake.

Q: Kodi cholinga chachiphunzitso chanu ndi chani?

M: Cholinga chathu nchiyani? Sindinakuuzeni? Kuti tiyende koposera dziko lino, kubwerera ku ufumu wa Mulungu kudziwitsa nzeru zako ndikukhala munthu wosinthika mmoyo.

Q: Ndipo kodi Karma imapezeka mmilingo yonse?

M: Osati yonse, kulekeza pamlingo wachiwiri basi chifukwa ubongo wathu, makina a kompyuta amakonzedwa mumlingo umenewo. Tikatsika kuchokera mmilingo yammwamba kuthupi lino kudzagwira ntchito. Mongaso master amatsika kuhokera mlingo wake kufika pamlingo wammusi kuti akathe kugwira ntchito.

Q: Munati pomaliza dziko lachiwiri tisananke mwamba kuti timasiya Karma yathu mmbuyo kapena kuyikonza. kodi izi zikutanthauzaso moyo wakale umene timakhala nawo mumoyo watsopano.

M: Inde chifukwa opanda kompyutayi palibe kulembetsa. Tili ndi Karma chifukwa cha kompyutayi imene ili ubongo wathu umene uyenera kulembera chinachiri chonse chotichitikira mdziko lino. Chifukwa chake tili nacho kuti tilembere zabwino kapena zoipa. Nchifukwa chake timatcha kuti Karma. Kodi Karma nchiyani? Zokuchitikira mmoyo zabwino, zoipa ndimmene timachitira tikakumana nazo. Koma chifukwa cha umunthu timadziwa kuti tiyenera kuchita bwino koma nthawi zina timapanga zoipa. Ndipo zoipazo zimatitsata ndikutilemetsa monga katundu nkutikanikitsa kukwera mapiri.

Q: Kodi zinalembedwa kuti tidzafika mlingo uti, tidzafika mlingo uti tikabadwa?

M: Ayi, tili ndi chisankho chothamanga kapena ayi. Monga tili ndi galimoto nde tathila malita 100 amafuta tikhoza kuthamanga kuti tikafike nsanga kapena kuyenda pang'onopang'ono. Zili kwa ife kusankha..

Q: Ndimangofuna kufunsa kodi angelo ali mlingo uti?

M: Ali mlingo uti? Zimatengera mtundu wake wa angelo.

Q: Angelo oyang'anira anthu.

M: Angelo oyang'anira akhoza kukhala mu mlingo wachiwiri. Angelo ali muni mwa anthu ndi oyitumikira.

Q: Kodi saposera pamenepa?

M: Ayi! Kupatula akasanduka anthu. Amachitira anthu nsanje chifukwa Mulungu amakhala mkati mwawo. Ife tili ndi upangiri wokhala amodzi ndi Mulungu. Anapangidwa kuti tikhoza kuwagwiritsa ntchito. Mwachitsanzo ngati chinalengedwa ndi Mulungu nde chinapangidwa kuti chidziti tumikira. Chitsanzo china mnyumba yanu muli zinthu zina zimene munapanga nokha kuti zifewetse moyo wanu. Monga mukhoza kukhala muno nkuyatsa magetsi ndikuwazimitsa, kuyatsa kanema ndi zina. Ngakhale zili zoposa inu eni ngati zikhoza kukhala malo amodzi nkuchita zinthu zingapo chinthu chimene simungachite ndi mphamvu zanu za kuthupi. Koma izi sizikutanthauza kuti ndi zoposa inu. Cholinga chake ndi kukutumikirani.

Q: Master Ching Hai, ndimafuna kudziwa kuti kodi pano mmene tili mthupi ndekuti tikhoza kukhala kuti tinagwa nkumasilidwa kwa thupili? Takhala tili chonchi kapena tinali pabwino.

M: Kusiya thupi nkunika mtsogolo? Eya tikhoza ngati tingathe. Pali njira zosiyira thupi nkupita mdziko likudza. Ena amapita pafupi, ena kutali enanso kumathero. Koma ndikafukufuku amene ndachita kuyambira ndili wang'ono njira yathuyi nde yofikitsa kumathero enieni. Pali njira zambiri zimene mukhoza kusankha kuti mutsate. Zilipo zambiri koma zochepa ndi zimene zimapita kumalecheleche a dziko. Komaso siambiri amene angapite mudziko lachisanu.

Nde njira yathu ndiyokutengerani kulachisanu tisana kumasuleni. Timaona ngati tikankera mwamba ndebwino koma sizili choncho. Ganizirani mutaitanidwa kunyumba yachifumu nde munapatsidwa chakudya chabwino kenaka mwati muzungulireko nkukaona dzala ndizina kapena mwakaona malo okonzera magetsi mmene munati muyendeko mwagwidwa ndi shoko nkumwarila nde nthawi zina sizonse zapatsogolo zimene zima khala zabwino.

Q: Ndili ndimafunso awiri loyamba nali kodi mbiri zakale zimachokera mdziko liti ngati tili nazo? Lachiwiri, kodi moyo wakale umagwirizana bwanji ndi Karma kodi zili mbali imodzi yazinthu zolemetsa?

M: Eya ndizogwirizana kwambiri. Funso loyamba kodi Karma imachokera kuti? Ukhoza kuwerenga zambuyo. Ndipo zonse zambuyo zimachokera ku zosungidwa za akashic. Iyi ili ngati musungira nkhani mdziko lachiwiri kwa aliyese amene akhoza kufikako. Sialiyense angapite ku malo osungira mabuku a United Nations koma ine ndikhoza kwa lero chifukwa nda itanidwa kuti ndidzalankhule koma inuso mukhoza chifukwa muli ngati okhala muno. Monganso tikalowa dziko lachiwiri tikhoza kudziwa mbiri ya munthu penanso tikalowa dziko loyamba tikhoza kuonako pang'ono za mbiri yakale ya munthu. Koma simakhala yapamwamba kapenaso yonse.

Nanga kodi mbiriyi imagwirizana bwanji ndi Karma yatsopano? Timati zimenezi ndi zimene taphunzira kuti tikathe kulimba mmoyo uno.

Timene mwaphunzira mmbuyo ndizimene zakufikitsani pamalo amene muli lero lino. Monganso zoipa zimene zinakuchitikirani mmbuyo zimakupatsanibe mantha. Mwachitsanzo ngati mumatsika masitepe nkugwa mmoyo wakale komaso kunali mdima mumati mukamatsika masitepe mumaopa kugwa nkudzivulaza ngati kalero. Monga Mozati amene anali katswiri ali ndi zaka zinayi anayamba kuimba piano ndipo pano akadali otchuka koma anamwalira asanafikepo mmoyo ndipo anali osakhutitsidwa kuti asiye luso lake chifukwa cha ichi anatsitsimuka ndipo luso lake lonse linamubwererela chifukwa anali ndi khumbo lopitiliza atamwalira.

Ndipo anthu ambiriwa amaphunzira zinthu zambiri mudziko la Astra asanabwerere kudziko lino. Ndipo amapatsidwa maluso oimba,

kafukufuku, kulemba ndi zinthu zina zimene anthu sadziwa. Amapanga zinthu zoti ena sanaganizepo kapena kulota chifukwa iwo anazona. Ndepali zinthu ziwiri zophunzira mdziko lino ndi lina. Iwo amphatso ndi luso ndi akatswiri adziko likudza monga la Astra dziko lachiwiri nthawi zina lachitatu ngati asankha kubwerera.

Q: Kodi mu mwambo wanu mulinji ndipo kodi kachitidwe kake katsiku ndi tsiku kamakhala kotani?

M: Poyamba ndikaulere komanso kopanda kumangika pokhapokha mudzimangilira nokha ngati mufuna kunka mtsogolo. Simuyenera kukhala mutayesapo kale yoga ndi zina. Koma mumalowa mu mgwirizano wosadya mazira ayi, mkako ndiololedwa ndi chinachilichonse chimene sichiphedwa kuti chidyedwe. Mazira ayi chifukwa ndikuphabe olo likhale losabala. Komanso amakonda kukoka mphamvu yoipa. Nchifukwa chake azamatsenga amagwiritsa ntchito mazira pochotsa matsoka kwa anthu aziwanda. Ngati mukudziwa (wina ayankha Eya). Mumadziwa nde zosangalatsa bola ndiri ndi umboni ngati ndilibe ndiri ndi chidziwitso chanu (kuseka).

Nthawi ya mwambo mumamva kuwala ndi mau aMulungu. Nyimbo yamzimu imakutengerani ku mlingo wina wa umunthu. Mukhoza kumvetsa kakomedwe ka samadhi-ntendere ndi chimwemwe chozama. Mukatha apo mukhoza kumakapanga nokha kunyumba. Ngati mumaliza ndikufuna kuti ndikuthandizeni nde ndikhoza. Chepetsani zonse zadziko mmenemo ndi mmene otsatira ambiri apitilizira atamaliza mwambo.

Q: Ine ndi maona ziwaliwali.....

M: Eee koma ziwaliwali zikusiyana ndi kuwala. Ziwaliwali zili ndi mitundu yosiyanasiyana nthawi zina kuda pena khofi pena chikasu kapena yofiyira. Zimatengera mmene alili. Koma mukaona munthu wa ziwaliwali zauzimu zamphamvu mumadziwa kuti nzosiyana.

Q: Ndilibe fuso koma ndinkapanga raja yoga kwa kanthawi nde ndimaganiza kuti ndinaona ziwaliwali nthawi imeneyo sindimazimvetsetsa.

M: Nde simumazona pano kapena mumazona kwa nthawi zina?

Q: Ayi ndinaleka kupanga mmbindikiro.

M: Nchifukwa chake munataya mphamvu zanu. Ngati mumakhulupilira mnjirayo mmbindikireso sizingakuonogeni.

Q: Ndinawerenga za zofunika kutsata. Kodi ukalandira mwambo umayenera kukhala molingana nazo?

M: Inde mene aja ndi malamulo a chilengedwe chonse.

Q: Sindikumvetsetsa chigololo.

M: Zikutanthauza kuti ngati muli ndi mwamuna kale osaganiza zopeza wina (kuseka). Khalani ndi moyo wosavuta wopanda zidangodango ndi zokhumudwitsa. Zimakhumudwitsa anthu ena. Sitikhumudwitsa anthu ena olo mmaganizo ndi mumtima. Timayesetsa kupewa mikangano, kuvutika kwa mtima, thupi, mmaganizo makamaka kwa okonedwa athu basi.

Ngati muli naye kale osamuuzwa. Zimapweteka kwambiri ukamuuzwa. Mungozikonza pang'onopang'ono ndi mwachete koma osamuuzwa. Chifukwa nthawi zina anthu amaona ngati ali ndi chibwenzi nkupita kunyumba ndikuuzwa akazi awo kapena amuna awo izi ndi kukhulupilila komanso za nzeru. Ndizopanda pake. Munalakwitsa kale mutengeranji nyasizo kupita nazo kunyumba kuti ena akazione. Ngati sakuzidziwa samamva kuwawa. Koma kudziwa kumapweteketsa mtima. Nde timakonza vuto nkuyesetsa kuti lisapezekeso.

Q: Ndaona kuti maMasta ambiri amakhala anthu oseketsa kodi pali mgwirizano wanji pakati pa kusangalatsa ndi moyo wauzimu.?

M: Ndikuona ngati amakhala okondwa ndi opeputsa zinthu. Nde amadziseka kapena anthu ena ndi zinthu zimene timakangamira nkuzitenga ngati zofunikira. Tikamaliza timamva kumasuka nde sititha kutengera chinthu pamgong'o. Ngati timwalira mawa timwalira ngati tikhala ndi moyo tikhala ndi moyo. Tikataya tataya yikapeza tapeza. Tili ndi nzeru ndi umunthu wotithangata mu zonse tikumana nazo. Nde sitiopa chilichonse. Timakhala opanda mantha nchifukwa chake timakhala mopanda phuma. Timamva wopatulika kwa dziko lino.

China chilichonse chimene timataya ndikupeza sichitanthauza kanthu kwa ife. Ngati tipeza zambiri zichitira ubwino anthu ndi abale. Sitimaona moyo wathu kukhala wopambana moti tingadutse muzowawa zadziko lino. Sizitanthauza kuti timangokhala koma

timagwira ntchito. Mwachitsanzo ndimagwirabe ntchito. Ndimachita zojambula ndi zamanja kuti ndipeze kangachepe.

